NAME OF CANDIDATE: ______________________________ EXAMINATION NUMBER ________________________________

# CHIMWALIRA ZONE EXAMINATION BOARD

## 2025 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE ZONAL MOCK EXAMINATION

# CHICHEWA

(100 MARKS)

**NAME:** (Surname First) ______________________________________________ **Time**: **1:00 – 03:15pm (2hrs 15min)**

**SCHOOL**__________________________________________________________ **DATE: 27th February, 2025**

## MALANGIZO

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba asanu ndi limodzi.**

2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: Gawo **A, B, C** ndi **D**.

3. Lembani dzina lanu ndi nambala yanu ya mayeso pamwamba pa tsamba lina lili lonse.

4. Lembani chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D**.

Lembani yankho la mu **Gawo A** pa pepala lomwe lili kumathero kwa mafunso a mu gawoli.

5. Yankhani mafunso a mu **Gawo B** ndi **C** m'mipata yomwe yaperekedwa pansi pa funso lililonse.

6. Yankhani mafunso a mu **Gawo D** pozunguliza lembo lokhoza pafunso lililonse.

7. Muchitebulo chilli pamwambachi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lilikutsogolo kwake.

8. Perekani kwa oyang'anira kulemba mayeso (imvijireta) pepala lonseli nthawi ikakwana.

| **Funso** | **Chongani zomwe mwayankha** | **Muno mu-salembemo** | |
|---|---|---|---|
| **1** | | | |
| **2** | | | |
| **3** | | | |
| **4** | | | |
| **5** | | | |
| **16 - 20** | | | |
| **21 - 25** | | | |
| **26 - 30** | | | |
| **31 - 33** | | | |
| **34- 35** | | | |
| **36 - 40** | | | |
| **41 - 43** | | | |
| | | | |

**GAWO A (30 MALIKISI)**

Yankhani funso limodzi lokha mwa mafunso ali m'munsiwa. Sankhani chimangirizo kapena kalata. Mawu a chimangirizo kapena kalata yanu asachepere 100 koma asapyole 150.

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu: KUSINTHA KWA NYENGO.Mwazina tsatirani izi polemba:

**Ndime yoyamba:**

- Zitsanzo za kusintha kwa nyengo.
- Zomwe zikuchititsa kuti nyengo isinthe.

**Ndime yachiwiri:**

- Mavuto omwe adza kamba ka kusitha kwa nyengo.
- M'mene mavuto akusintha kwa nyengo akhudzira miyoyo yathu.
- M'mene mavuto akusintha kwa nyengo akhudzira dziko lapansi.

**Ndime yachitatu:**

- Zomwe tingachite kuti tithane ndi mavuto akusintha kwa nyengo.

**KAPENA**

**2.** Lembani kalata kwa mphunzitsi wamkulu wa Mwayi sekondale sukulu,P.O.Bokosi 5027, Ntcheu.Muwafotokozere kuti mwalephera kupita kukayamba Folomu 1.

**Ndime yoyamba**

- Tchulani dzina la zaka zanu.
- Kodi ndinu mnyamata kapena mtsikana?
- Chaka chomwe mwasankhidwa.
- Sukulu yomwe mumkaphunzira.
- Nambala yanu nthawi yomwe munkalemba mayeso.

**Ndime yachiwiri**

- Tchulani chifukwa chomwe mwalephelera.
- Mupemphe kuti akusungileni malo.

**Ndime yachitatu**

- Ndani angakuchitireni umboni pa pempho lanu?
- Chisangalalo chanu chidzakhala chotani akakusungirani malo.

**GAWO B (MALIKISI 20)**

**3. Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo.**

Kalekale m'dziko la Kampala mudali mfumu yotchedwa Nagoli yomwe idali yolemera kwambiri.Mfumuyi idali ndi ana awiri,woyamba ankatchedwa Kanthiti ndipo wachiwiri adali Gwaza.Mfumu Nagoli idali ndi zifuyo zochuluka monga ng'ombe,mbuzi,nkhuku,abakha ndi nkhunda.Pakhomo pake padali pamwanaalirenji.Ponena mwatchutchutchu idali Mpondamatiki.

Mwadzidzidzi mfumu Nagoli idadwala koopsa ndipo idayitanitsa ana ake onse kuti ikambe nawo.Iyo idapempha ana ake aja aliyense anene zokhumba zake iyo idakali moyo.Kanthiti adali woyamba kunena zakhumbo lotenga chuma chonse cha atate ake.Gwaza ndiyemwe adanena zakhumbo lake lenileni lomwe lidali lakuti atate ake achire.Choncho,mfumu Nagoli idatenga ndodo ziwiri nipereka imodzi kwa mwana aliyense.Iyo idawalimbikitsa anawo kuti aliyense akasungitse ndodo yake.

Madzulo a tsikulo Kanthiti adavutika mumtima.Adatenga ndodo ija nayithyola ndi kuiponya pa moto.Iye adawadandaula atate wake chifukwa chomupatsa ndodo mmalo mwa chuma.M'mawa watsikulo mfumu Nagoli idainitsa nduna zake zonse,mikoko yogona,achibale,mkazi ndi ana ake.Iyo idauza gulu lonse kuti asadzalimbane patsogolo.Mfumuyi idauza mwana wake Kanthiti kuti atenge ndodo yake ndi kuloza chomwe akufuna.Apatu kanthiti adangoti kakasi.Iye adayamba kulira nakalowa mnyumba mwake.Mfumu itamva zomwe Kanthiti adachita ndi ndodo yake ija,idauza Gwaza mwana wake wina kuti akatenge ndodo yake ndikuloza zomwe akufuna.Gwaza adatenga ndodo yake ndipo adaloza chuma chonse pamodzi ndi atate ake.Pa ichi mfumu idauza mwana wake Gwaza kuti chuma chomwe waloza chidzakhala chake komanso poti waloza iye mfumu,ufumunso udzakhala wake iyo ikadzamwalira.Anthu adaomba mmanja ndipo nthungululu zidamveka ponseponse.

**Tsopano yankhani mafunso otsatirawa pa mizere ili pansi pa funso lililonse.**

**a.** Kodi mfumu Nagoli inkakhala kuti? ( malikisi 1)

________________________________________________________________________________

**b.** Nchifukwa chiyani mfumuyo idaitanitsa ana ake? (malikisi 2)

________________________________________________________________________________

**c.** Tchulani zinthu ziwiri zotsimikiza kuti mfumu Nagoli idali yolemera. (malikisi 2)

________________________________________________________________________________

**d.** Kodi Kanthiti ndi Gwaza adalandira chiyani kuchokera kwa atate awo? ( malikisi 1)

________________________________________________________________________________

**e.** Nchifukwa chiyani Kanthiti adakhala ovutika mumtima mwake? (malikisi 2)

________________________________________________________________________________

**f.** Fotokozani cholinga chenicheni cha mfumu Nagoli poitanitsa gulu la anthu pamodzi ndi banja lake.

________________________________________________________________________(malikisi 2)

**g.** Perekani matanthauzo amawu otsatirawa:

(i) mikoko yogona______________________________________________________(malikisi 1)

(ii) adangoti kakasi_____________________________________________________(malikisi1)

**h.** N'chifukwa chiyani Kanthiti adalephera kulandira chuma kuchokera kwa atate ake? (malikisi 2)

________________________________________________________________________________

**i.** Tchulani zinthu ziwiri zomwe Gwaza adalodza. (malikisi 2)

________________________________________________________________________________

j.N'chifukwa chiyani kudamveka nthungululu ndi mmanja patsiku lija? (malikisi 2)

________________________________________________________________________________

k.Perekani mutu woyenera wa nkhaniyi. (malikisi 2)

________________________________________________________________________________

**GAWO C. (MALIKISI 10)**

**4.** Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawa .

**"Ine ndati ndidzacheze nanu nkhani ya Nasiyani.Limbikani wandiuza kuti Nasiyani mwamuletsa sukulu.Choti mudziwe ndi chakuti, mtsikanayu amachita bwino mkalasi komanso ndi wamakhalidwe abwino kusukulu."**

**Mafunso**

**a.i**.Angayankhule malonjewa ndi ndani? (malikisi 1)

______________________________

ii. Malonjewa akuchitikira kuti? (malikisi 1)

______________________________

______________________________

iii.Mungawalangize chani makolo oletsa mtsikana kupita ku sukulu? (malikisi 2)

______________________________

______________________________

**b.** Fotokozani njira imodzi yopewera nthenda ya kolera. (malikisi1)

______________________________

______________________________

**Kupanga ziganizo**

**Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:**

**a.** chola (malikisi 1)

______________________________

**b.** mliri (malikisi 1)

______________________________

**c.** balamanthu (malikisi 1)

______________________________

**d.** psu (malikisi 1)

______________________________

**e.** tsuka (malikisi 1)

______________________________

**GAWO D (MALIKISI 40)**

**Mafunso 6 mpaka 10 :Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

**6.** <u>Zopsetsa</u> zimakoma.

**A.** dzina **C.** mlowammalo
**B.** mneni **D.** mfotokozi

**7.** Ndiwo <u>zamasamba</u> zimapatsa thanzi.

**A.** dzina **C.**mfotokozi
**B.** mneni **D.** mperekezi

**8.** <u>Makono</u> anthu ambiri ndi odzikonda.

**A.** muonjezi **C.** mfotokozi
**B.** mneni **D.** dzina

**9.** Mbuzi zija <u>zili</u> m'khola.

**A.** dzina **C.** muonjezi
**B.** mneni **D.** mfotokozi

**10.** <u>Hehede!</u> Zoseketsa odwala.

**A.** mvekero **C.** dzina
**B.** mneni **D.** mfuwu

**Mafunso 11 mpaka 13 .Perekani chachikazi cha mayina awa.**

**11.** A Yolofati apita kwa <u>atatavyala</u> awo.

**A.** amalume **C.** azakhali
**B.**agogo **D.** apongozi

**12.** <u>Chipsolopsolo</u> changa chajiwa.

**A.** tambala **C.** thadzi
**B.** msoti **D.** mkota

**13.** Yosefe adali <u>Kapolo</u> mdziko la Iguputo.

**A.** bwana **B.** dona
**B.** mdzakazi **D.** wantchito

**Mafunso 14 mpaka 18: Sankhani mawu amene akufanana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

**14.** Kwathu kuli <u>gule</u> wosangalatsa

**A.** chamba **C.** malipega
**B.** nyau **D.** ng'oma

**15.** <u>Kabawi</u> wagwira mwanapiye.

**A.** kamtema **B.** khwangwala
**B.** katawa **D.** nkhwazi

**16.** Mayi Jusa amalima <u>mawere</u>.

**A.** lipoko **C.** nandolo
**B.** nsawa **D.** mapira

**17.** Ambewe amaweta <u>mberere</u> zambiri.

**A.** nkhosa C.ng'ombe
**B.** mbuzi D.nkhanga

18. M'munda mwawo muli <u>gang'a</u>.

**A**.chiswe **C**.udzu
**B**.ngumbi **D**.chimanga

**Mafunso 19 mpaka 23: Sankhani nthawi za aneni omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.**

19. Nkhuku za a Ngozo <u>zikumwa</u> madzi.

A.Nthawi yangothayi
B.Nthawi yatsopano yopitilira
C.Nthawi yakawirikawiri
D.Nthawi yopitilira

20. <u>Ankavina</u> bwino akali wamphamvu.

A.Nthawi yopitilira
B.Nthawi yakale yopitilira
C.Nthawi yatsopano
D.Nthawi yakawikawiri

21. Ndikakhoza mayeso a boma adzandisankhira ku sekondale.
 A.Nthawi yatsopano
 B.Nthawi yopitilira
 C.Nthawi yamtsogolo
 D.Nthawi yatsopano
22. Akukamba nkhani mofatsa.
 A.Nthawi yakale
 B.Nthawi yatsopano
 C.Nthawi yatsopano yopitilira
 D.Nthawi ya mtsogolo
23. Nasimango amavala nsapato yokongola.
 A.Nthawi yakale
 B.Nthawi yatsopano
 C.Nthawi yakawirikawiri
 D.Nthawi yangothayi

**Mafunso 24 mpaka 25: Sankhani msintho wa aneni omwe walembedwa bwino pogwiritsa ntchito 'yala' pamisintho iyi.**

24. wotsutsa
 A.yalayala B.yalitsa C.yalula D.yalidwa
25. womuchitira
 A.yaliridwa B.yalula C.yalira D.yalidwa
26. wobwerezabwereza
 A.yalula B.yalulayalula C.yalayala D.yaliridwa
27. wochititsa
 A.yalula B.yaliridwa C.yalitsa D.yalitsitsa
28. wochititsitsa
 A.yalitsa B.yaliridwa C.yalitsitsa D.yalula

**Mafunso 29 mpaka 33: Sankhani mikuluwiko yomwe matanthauzo ake ndi ofanana ndi a yomwe mwapatsidwa**.

29. Kwa eni kudyetsa nthanga dzungu ukulifuna
 A.Mutu umodzi susenza denga.
 B.Ukayendera ntchire wayendera zonse.
 C.Zengerezu adalinda kwawukwawu.
 D.Kwa eni kulibe mkuwe.
30. Chibale mchipsera sichitha
 A.Kachipande kathelere kakoma nkuyenderana.
 B.Chibale ndi fupa sichiwola.
 C.Katungwe mkukankhana.
 D.Konza kapansi kuti kam'mwamba katsike.
31. Mako ndi mako usamuwone kuchepa mwendo
 A.Ukapanda mano usamaswe phale.
 B.Timba sachepa ndi madzira ake.
 C.Walira mvula walira matope.
 D.Suzumire adaphetsa mkhalakale.
32. Mphungu sataya nthenga
 A.Munthu wadyera C.Munthu womana
 B.Munthu wodzikonda D.Munthu wabodza
33. Chalaka nyani chili ndi khambi
 A.Chomwe walephera munthu wodziwa palibe angathe.
 B.Chomwe chakanika wamkulu mwana sangathe.
 C.Chomwe chakanika mphunzitsi,wophunzira sangathe.
 D.Chomwe wamkulu watola mwana sangatole

**Mafunso 34 mpaka 36: Sankhani matanthauzo oyenera a zining'a zomwe zatsekedwa mzere kunsi m'ziganizo zotsatira.**

34. Iye uja ndi Pakome ine.
 A.Munthu wochita zinthu kuti awononge.
 B.Munthu wochita zinthu kuti zikome.
 C.Munthu wochita zinthu kuti amukonde.
 D.Munthu wochita zithu kuti akonze.
35. Amalume pano adalowa chamwaka.
 A.Kulowa chinamwali
 B.Kukhala wosokoneza
 C.Kukhala wodwaladwala pafupipafupi
 D.Kukhala wodzitengera
36. Chaka chino ndikuwonetsa buluzi wang'ala.
 A.buluzi wosaona C.mtendere
 B.mavuto D.mazangazime

**Mafunso 37 mpaka 40: Pezani mawu amene ali ndi zizindikiro za mkalembedwe zoyenera**

37. A .Ha? Mwanawe, andithangate ndani?
 B. Ha! Mwanawe andithangate ndani?
 C. Ha! Mwanawe, andithangate ndani?
 D. Ha,Mwanawe,andithangate ndani?
38. A.Kodi wadya! C.Kodi, wadya!
 B.Kodi wadya? D.Kodi? wadya.
39 A.Abambo adati, “Choka iwe mwana,wakuba.”
 B.Abambo adati, “choka iwe mwana wakuba.”
 C.Abambo adati, “choka iwe mwana wakuba!”
 D.Abambo adati,” choka iwe mwana wakuba.
40. A.Aphunzitsi anena kuti tisalongololе.
 B.Aphunzitsi anena, kuti tisalongolole.
 C."Aphunzitsi anena” kuti tisalongolole.
 D."Aphunzitsi anena kuti tisalongolole.”

**Mafunso 41 mpaka 45: Sankhani nthambi za chiganizo**

41. Sindikusiya mpaka undidalitse.
 A.Ya muonjezi C.Ya dzina
 B.Ya mfotokozi D.Yoyima payokha
42. Sizowona kuti chaka chino kuli chilala.
 A.Ya mfotokozi C.Yoyima payokha
 B.Ya dzina D.Ya muonjezi
43. Zoti amayi abweranso sizikudziwika.
 A.Ya mfotokozi C.Yoyima payokha
 B.Ya muwonjezi D.Ya dzina
44. Ngakhale wabwera kwathu sindikupatsa ndalama zako.
 A.Ya dzina C.Yoyima payokha
 B.Ya mfotokozi D.Ya muonjezi
45. Jese watenga nsalu imene adamugulira.
 A.Ya muonjezi C.Yoyima payokha
 B.Ya dzina D.Ya mfotokozi

MAFUNSO ATHERA APA……………….